

Uzimu Weniweni - Zolembedwa mu Chichewa

Gawo 1: Maloto a Mulungu pa Moyo wanu

Zolembedwa ndi Chip Ingram

Ndikufuna mudziwe kuti kholo lililonse limakhala ndi loto la mwana wake. Ndikufuna muganizire mobwerera m'mbuyo pang'ono, ngati muli kholo ...ndipo ngati simuli, mwina mwake muganize za chimene makolo anu ankaganiza pomwe munabadwa. Kholo lililonse ndikufuna mubwerere kwa mwana wanu woyamba kubadwa [chisamba chanu]. Munalibe mwana aliyense ndipo akazi anu anali woyembekezera, kapena munali mkazi ndipo munali woyembekezera ndipo ganizirani zinthu zonse zimene zinautsa mmaganizo anu zokhudza mmene mwana wanu wamwamuna kapena wamkazi angadzakhalire ndi maloto onse, maganizo, ziyembekezera ndi zokhumbira.

Ndipo chimene ndikufuna kukuuzani ndi chakuti Mulungu ali ndi loto kwa ana Ake. Koma chimene timachita ndi chakuti timapeza zau Mulungu ndipo penapake timaganiza kuti lye ali wamphamvu zowopsa komanso pali malamulo ndi ndondomeko zoyenerenza kukhalira. Ndipo kwa inu kuti mugwire zokhudza za m'mene Mulungu amamvera, ndikufuna kugawana nanu mwachidule kwambiri ndi nkhani yanga yokhudza mmene ndinamvetsera mmene Mulungu mozama amadzala chikhumbo ndi maloto kwa ife.

Chinali chisamba chathu cha Theresa ndi ine mwini. Tinali kuphwando ndipo Theresa akuti, "Chip, yakwana nthawi", ndinati, "Theresa, tiyeni." Mukudziwa, simudziwa chimene mukuchita. Matenda anali atayamba kuchitika kwa pafupifupi maora atatu. Tinapita kunyumba, kukatenga katundu wathu ndipo tinapita ku chipatala cha Baylor. Kwa maora 27 otsatira, Theresa tikhala tili limodzi. Matenda anali otenga nthawi yayitali. Panali zinthu zina zovuta.

Kwa zifukwa zina zingapo, sakadatha kuchotsa mwana. Anapeza kuti china chake chinali cholakwika. Anayika makina owunikila mwana m'mimba mwa mkazi wanga ndipo ndinakhala pansi pa mbali pake kwa maora 27 ndi makina owunikira pa mwana... ngati mukudziwa mmene mtima wa mwana umagundira umagunda chonchi – gu,gu,gu, gu. Ndipo kenako amakhala ngati matenda ayambaso kenako mtima mkudzagundanso gu,gu, gu gu. Adokotala ndi anamwino amabwera akuthamanga. Gu gu,gu, gu.

Tinadutsa mu izi pafupifupi katatu mmaora 27. Pakatha pafupifupi maora asanu ndi atatu aliwonse timayima ndipo tinapemphera, kulira ndi kupereka mwana wamwamunayo kwa Mulungu. Ndipo ndinaganizira kuti, "Mwina tikhoza kukhala naye kapena ayi." Ndipo kenako ndinayamba kuganizira za Theresa ndi kuti mwina sindingakhale nayenso. Kodi chimene chingachitike ndi chiyani?.

Ndi maora 27 amenewo ndinali ndi nthawi yoganizira za maloto onse amene ndinali nawo okhudza mwana wamwamuna amene anabwera poyera - kuti mwana wamwamuna amene ndinaganizira kuti atha kutayika. Ndipo ndikufuna kuti inuyo mudziwe kuti china chake pansi pa mtima wanga chinali chochititsa mantha kwambiri ndi kulira pa chimene ndikadataya.

Mwana wamwamuna anabadwa patatha maora 27. Theresa anali atapuputidwa, ndikuganiza ananena kuti. "Ha!" Ndipo kenako anayika khandalo mmanja mwanga. Anali amodzi mwa malo amene amaganiza bwino kuti bambo a mwana anali wofunikira kwambiri, ndipo ndinakhala ndi mwana wanga wamwamuna kwa theka la ora limodzi. Ndinanyamula khanda limenelo ndi misozi ikutsika mmaso mwanga, kuganizira, "Sindinadziwe kuti izi zichitikadi," ndipo ndinaganizira za maloto onse omwe ndikanataya.

Ndimakumbukirabe panali pansi ponyenzimira, ndipo ndinali ndi mtima wothokoza. Ndikukumbukira nditagwada mawondo anga pansi ponyenzimirapo, nditananyamula mwana wanga wamwamuna, ndikungolira ndi kuyamika Mulungu.

Ndipo ndikufuna kuti mudziwe - chifukwa chake ndinapangidwa mu chifanizo cha Mulungu. Ndipo chophatikizidwa mkati mwa mtima wa bambo ndi kuphatikizidwa mkati mwa mtima mwa mayi ndi loto ndi khumbo la ana anu chifukwa Mulungu anakupangani inu. Ndipo umu ndi m'mene lye amamvera zokhudza inu.

Ndipo ambiri mwa ife pamene ana athu akadali ang'ono ndi kuti ndife makolo achichepere osakhwima - timakhala ndi maloto munga, "Ndimalakalaka atakhala osewera mpira wa miyendo", kapena, "ndimalakalaka atakhala oyimba," kapena "zidzakhalabwino kwambiri akadzakhala othamanga kapena waluso lina lapadera..." Ndipo kenako, mukamakula pang'ono ndipo amadutsa misinkhu ina ya moyo ndiye mumanena kuti, "Chabwino, ndikulakalaka kuti mwina adzapeze ntchito yabwino." Kapena "Adzachite bwino sukulu." Ndipo maloto ambiri amakhala okhudza za zimene adzachite.

Kenako mukayamba kukula ndi nawonso akukula mumafika pakuti mumanena kuti, "Sindisamala za chimene akuchita. Ndingofuna mwana amene amandikonda, amakonda Mulungu, ndipo amanena chilungamo." Maloto anu amatembenuka kukhala adzakhalamunthu wotani uyu, chifukwa apa ndi pamene ndikuwuzeni mwakuthekera konse chimwemwe chanu chachikulu chimene mudzakhalenacho pano pa dziko lapansi chidzakhalubale wanuwabwino ndi mwana wanu. Ndipo chowawitsa mtima kwambiri ndi chopweteka kwambiri chimene mungathe kukumana nacho ndi chokhudza ana anu.

Palibe amene angakukhumudwitseni kwambiri kuposera ana anu. Ndi gawo la inu. Mtima wanu ndi wolumikizana ndi wawo. Ndipo ndikhoza kutenga chimkuzamawu ndi kuchiyendetsa muno ndipo tikhoza kutenga nkhani zokhudza ana athu amene anapanga chisankho choipa kapena ana athu amene ali muzizolowezi zoipa zokanika kusiya kapena ana amene anasiya kukulankhulani kapena ana amene ndi... lembani mmizere yopanda kanthupa.

Kodi ndi angati mwa ife amene tinganene kuti, "Sindigasamale olo pang'ono za sukulu imene akuphunzira, sindingasamale olo pang'ono kuti ndi ntchito yanji imene akugwira; ngati tili ndi ubale wachikondi, ndipo ngati akula, ndife abwenzi, sindingasamale za zina zotsala," tingatero? Chifukwa pakutha pa nthawi, loto lenileni mtima mwanu silakuti ana anu amachita chiyani ndi zokhudza kuti akula kukhala ndani ndipo ndi zokhudza ubale wawo ndi kulumikizana kwenikweni ndi inu.

Ndikufuna kuti mudziwe ichi -Atate wathu wammwamba ali ndi loto la kwa aliyense wa ana Ake, ndipo loto la Mulungu ndikukupangani inu munga-----Ake - lembani mau akuti - mwana. "Mukhale okhwima kapena kukwaniritse mmene anakupangirani." Mateyu 5:48 akuti, "chifukwa chake inu mukhale angwiro munga Atate wanu a Kumwamba ali wangwiro."

Mu Aroma 8:29 Paulo akuti Mulungu amagwiritsa ntchito china chilichonse chochitika, chosangalatsa, chotsika, ubale uliwonse, chuma chilichonse chimene tingadutse kutisanduliza kukhala muchifanizo cha mwana wake. Mu Aefeso 4 akunena kuti cholinga chathunthu cha mpingo chinapangidwa kotelo kuti kudzera mmaubale amene tili nawo ndi mphatso zimene Mulungu amaika muthupi kuti tonse tikule mu mulingo wa thupi wokula musinkhu wathuwathu wa Khritsu.

Mukufunika kumvetsetsa- choyambirira moyo wanu ndi Atate wanu wa Kumwamba siwokhudza zimene mmachita, kapena kukhudza zimene mungakwaniritse, osati kukhudza ntchito imene mmagwira, osati mumapeza zochonga zingati muuzimu. Loto Lake loyambirira ndikuona kuti inu mwakhala munthu otani, muli ndi ubale wotani ndi iye. Amafuna kuti inu mukhale okonda, wokoma mtima ndi wofatsa, munthu woyera amene amayenda mwachikhulupiriro. Amafuna kucheza nanu ndipo amafuna kuti inu mumuyankhule. Pamene mwaifika pa kakasi wakuti mupange chiganizo ndipo aliyense akuti chitani ichi ndipo Atate wanu wa Kumwamba akuti chitani icho amafuna kuti inu munene kuti, "Atate ndikufuna kuchita munjira yanu. Ndikufuna ndikukondweretseni." Amafuna ubale wabwino, wachikondi chakuya ndi inu.

Mwatsoka, mutsiku lathu, tili ndi mavuto akulu mu Chikhristu. Chinachake chachitika muzaka 40 mpaka 60 za m'mbuyomu zimene sizinachitikepo, ndi zowopsa kwambiri ndi zodabwitsa. Muona kuti, miyandamiyanda ya anthu yabwera kwa Khristu muzaka 40 mpaka 60 zapitazo kuposera zaka mazana awiri kapena atatu zapitazo.

Uthenga Wabwino wazungulira dziko lonse lapansi kuposa kale lonse. Anthu ambiri anena molimba mtima kuti "Ambuye Yesu, ndikuzindikira kuti ndinu Mulungu wa dziko lonse lapansi. Munalipira machimo anga munawuka kwa akufa. Ndikukukhulupirani." 'Ndipo amalowa mu mitima yawo.

Koma mawu a John stott, namandwa wakale amene anayenda kuzungulira dziko lonse lapansi anati, "Chikhristu sichinakuleko monga mmene chakulira mzaka zophatikiza makumi anayi kapena asanu zapitazo. Koma ndi mtunda wotalikana kwa pafupifupi mailosi 16 miliyoni ndipo kukhutala kwake kufana ka 16 ya inchi imodzi." Iye anati, "Chosowekera kwambiri mu Chikhristu lero, mudziko lililonse kupatula kumene akhristu amakanthidwa kapena kuphunzitsa akhristu kukula mokhazikika, ndi kukhwima mu uzimu."

Kodi maripoti onse komanso chiwerengero ndi zina zambiri zimene taziona zimatiuza chiyani? Mwa anthu 10 alionse 8 amanena kuti ndi akhristu ndi ofanana pang'ono zedi ndi banja. Kodi mukudziwa chimene ine ndi kunena? Pamene ndinu wokhwima muuzimu, mumaganiza monga Yesu, ndipo mumayenda ngati Yesu, ndipo mumakonda ngati Yesu, ndipo ndinu wosadzikonda ngati Yesu, ndipo zinthu zoyambirira mmoyo wanu ndi ndalama zanu ndi nthawi yanu zili ngati Yesu akukhala mthupi mwanu.

Koma kwa khwimbi la anthu, miyanda yambiri, mawu awo ndi dongosolo la nzeru za chikhulupiriro chawo okhudza Yesu ndi Mulungu zili pamwamba ndipo makhalidwe a moyo wawo ali pamwamba. Ndi chifukwa chake pali anthu ambiri amene ali panja pa Khristu ndikumayang'anira Chikhristu ndi kumaona mipingo ndi kumakumana ndi anthu amene ndi otsatira Yesu enieni amanena, "Kodi mukudziwa china chake? Ngati chili chimenecho, sindikuganiza kuti ndichifuna."

Ndikuganiza kuti chosowa kwambiri lero mdziko lapansi ndi chakuti Akhristu adzikhala monga Akhristu. Apa ndiye pali posangalatsa. Sizongolota, sizakuti tikuyesetsa. komanso sizongokhala wa chipembedzo. Mulungu amapereka chithunzi chomveka bwino pa loto lake zokhudza moyo wanu mu Aroma 12. Loto la Mulungu kwa mwana aliyense ndikukhala ophunzira kapena otsatira wa Khristu - ndipo mungathe kulemba - Mkhristu wa mu Aroma 12. Ichi ndi chifuniro chake.

Chifuniro chake pa mwana aliyense wa Mulungu pamaso pa dziko lapansi, kusatengera kumene akuchokera, mtundu, mwamuna kapena mkazi, mpingo - khumbo la Mulungu, Chifuniro cha Mulungu kwa otsatira aliyense ndi chakuti akhale Akhristu apa Aroma 12.

Tsopano sindikuti Aroma 12 ndi zokhazo zimene otsatira angakhale koma chimene ndikunena pano ndi ichi. Ndikunena kuti ndi kuwomba mkota chabe. Ndi chithunzithunzi. Ndi maganizo odabwitsa amene Mulungu anapereka kwa mtumwi Paulo. Akutenga ziphunzitso zonse za Yesu ndipo kwa mitu 11, akulemba zokhudza ntchito ya Khristu ndi tchimo la mtundu wa munthu ndi zauMulungu. Ndipo kwa mitu 11 akulemba zokhudza zonse zimene Mulungu wakhwaniritsa ndi kukula kwa chikondi chake kwa anthu.

Kenako mmutu 12 Paulo wayima ndi kutipatsa ife chithunzithunzi, chithunzi chimenechi chamsanga.

Zili ngati ena mwa anthu a za malonda amene amakhala ndi dongosolo labwino la chinthu chatsopano chimene akufuna chipite pa msika. Dongosolo likhoza kukhala ndi masamba 20 kapena 50 kapena 80 a kafukufuku amene apanga zokhudza chinthu chawo. Koma muzaka zomwe ndaona zinthu ndikayankhula ndi anthu amenewo ndipo amene ali ndi chinthu sangafotokoze mowomba mkota mutsamba limodzi kapena masamba awiri a dongosolo lonse-

kuti chinthucho ndi chiyani chimene akufuna kuchita mmene akufuna kuchitira - mmene akufunira kuti chichitidwe - dongosolo lawo silingawerengedwe nkomwe.

Mu Aroma 12 mtumwi Paulo akupereka mowomba mkota za chimene chikutanthauza kukhala wauzimu weniweni. Chimene tiphunzire pamene tikudutsamo, choyambirira - ndinu wokonzekera ichi - **ndizolumikizana**. Yang'anani notsi zanu. Kodi mungatenge notsi zanu ndikungoziyangana zili zotsegula? Ndipo ngati muli ndi cholemba zungulizani mawu a mfungulo pamene tikudutsa mundimeyi. Zonse zimene tichite ndikupereka mwachidule ndipo tidzazama mmagawo onse palokhapalokha.

Likuti, "Ubale ndi Mulungu." Muzungulize mawu akuti, "Mulungu." Ndime 1 ikulankhula za chithunzithunzi cha kukhwima muuzimu, za uzimu weniweni ndi Mulungu. Kenako mutsike mmunsi ikunena kuti ndi ubale ndi dziko lapansi. Muzungulize mawu akuti, "dziko lapansi." Pali dongosolo la dziko lapansi limene tiphunzire zokhudza chikonzero cha dziko lapansi limene limapatsidwa mphanvu ndi mdani wa moyo wathu, kufuna kukukopani kuti muchotse chikondi chanu cha Khristu.

Ndipo kenako lidzakamba za ubale wanu ndi inu eni ake. Zungulizani mawu akuti, "inu eni ake." Tiphunzira pang'ono patsogolo kuti Mulungu akufuna inu mukhale kudzifufuza kwachindunji ndi kodekha. Kenako zindikirani kuti tikukamba za ubale okhulupirira. Zungulizani mawu akuti, "okhulupirira." Pali njira zina zimene otsatira enieni okhwima muuzimu amalumikizana ndi Akhristu ena imene imachita zinthu zodabwitsa mwa iwo ndi zinthu zodabwitsa mwa ena.

Kenako pomaliza zungulizani mawu omaliza. Ndi ubale ndi, "osakhulupirira." Pali njira imene anthu amene amakonda Yesu imene mzimu wake umakhala mkati mwanu, amayankhira ku zolakwa zokhoma zolimba, zovuta zowawa zimene zimabwera mmoyo mwanu.

Chinthu chachiwiri chimene muphunzire zokhudza mkhritsu wa Aroma 12 ndi chakuti ndi **zochitika** ndi kuti ndi **zoyeseka**. Ichi sichikungokhala zokumva zauzimu zokha. Tsatirani nafe ngati mungathe. Zindikirani chimene ndime ikunena. "Chifukwa chake ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera."

Mawu awa akuti, "mupereke" ndi a kanthawi ina yake. Ndipo chimene akudzanena pano ndi chimene mungadziwe chochitika ndi choyeseka. Wotsatira weniweni wokhwima muuzimu ndi wodzipereka kwa Mulungu. Pa tsiku lina, pa nthawi ina yake moyo wa ulendo wanu wauzimu, bambo kapena mayi, kapena mwana wa sukulu anazindikira mmene ukulu ndi mphanvu za Mulungu zilili, ndi kuti mwagwada pa mawondo anu ndi kuweramitsa mtima ndi kunena kwa Mulungu, "Ine ndili mu zonse. Ndidzachita chilichonse chimene mukufuna ine kuti ndichite. Mawu anu adzakhalo mlozo wa moyo wanga. Ndikufuna kukonzanso moyo wanga, maubale anga ndi zinthu zimene ndimazona zofunika kwambiri mozungulira chili chonse chimene mudzanena."

Ndipo ichi chiyankha limodzi la mafunso akuluakulu amene mudzakumana nawo mmoyo mwanu. Ndipo funso limenelo ndi ili - **Kodi mungampatse bwanji Mulungu chimene lye akufuna kwambiri?** Kodi munayamba mwaganizapo za izi? Mulungu ndi munthu. Iye ali mphanvu za umunthu zosawoneka. Iye ndi munthu. Ndipo ngati muli ndi bwenzi wabwino ndipo ali ndi tsiku limene anabadwa, mumadzifunsa mafunso akuti, "Kodi chimene angafune ngati mphanvu ndi chiyani?" Kapena ngati ndinu wokwatiwa kapena wokwarira, mumati, "Kodi chimene mnzangayu angafune kwambiri ndi chiyani? Kapena ngati ndinu makolo, "Kodi chimene ndingathandizire ana anga ndi chiyani?"

Kodi munayamba mwadzifunsa nokha, "Kodi chimene Mulungu akufuna kwambiri kuchokera kwa ine ndi chiyani?" Ndipo kodi mukudziwa chimene mudzaphunzire? Akufuna inu. Osati zochita zanu za chipembedzo. Pali malo akusanduliza Baibulo, pali malo a mpingo, pali malo a pemphero, pali malo a zinthu zina zosiyanasiyana. Koma mutha kuchita zonsezo ndi kusapereka moyo wanu kwa lye.

Mukuona kwanga mu miyoyo yambiri ya Akhristu, pali chida chimodzi chosoweka. Aroma 12 siyokhudza ubale wokha ndi zochitika, ikuyankha funso ili lalikulu ndi kuperekanso chida chimene chikusowekanso mu ubale uli wonse. Ndipo chida chosoweka kwambiri mmoyoyo ya Akhristu - ndipo mukuyenera kulemba ichi kumbali kwa notsi zanu ndi - **mphamvu**. Ndife operewera. Akhristu ambiri amayesetsa kwambiri.

Ndikukumbukira ndinalandira email pomwe tinaphunzitsa maphunziro awa kwa masiku angapo pa waillesi mnzaka za mmbuyozo ndipo tinali ndi zikwizikwi za email ochokera kwa anthu amene anaphunzira izi. Takhala ndi magulu ang'onoang'ono mu America ndi kuzungulira dziko lonse lapansi amene amaphunzira maphunziro awa, choncho ndili ndi kafukufuku. Ndipo pali email imodzi imene ndikukumbukirabe kuwerenga ndi kuganiza, "Heee!"

Mzimayi ananena "Ndinali ku khitchini kutsuka mbale, ndipo mmawa umenewo ndinadzuka ndikumva ngati ndili kutali ndi Mulungu. Ndakhala ndili Mkhristu kwa zaka 22. Koma pa zifukwa zina ndinadzifunsa ngati mnzanga wina aliyense angandifotokoze, ngati angagwiritse ntchito mawu akuti, 'Mkhristu wabwino' kapena 'wina wake amene amakondadi Mulungu ndi dzina langa'".

Ndipo anati "Mukudziwa, ndayesetsa, ndalephera, ndayesetsa, ndalephera, ndikuyesetsa. Ndikudziwa kuti ndine wobadwanso mwatsopano. Ndakhala mkhristu zaka 22. Ndili ndi vuto la mowa ndipo ndili ndi vuto la khalidwe loyipa ndi vuto la zolaula. Ndipo sindikonda chimene ineyo ndili.

"Ndipo maganizo odzimva ochimwa amenewo chifukwa cha mmene ndimakhalira moyo wanga anayamba kutuluka. Ndipo ndikutsuka mbale, ndipo wayilesi inali yotsegula ndipo uthenga ukubwera wokhudza mkhristu wa Aroma 12, ndipo kunali pa kudzipereka."

Ndipo anati, "Pamene ndimatsuka mbale, misozi imatsika mmaso mwanga, "Ndipo anati "ndinali ndisanamvepo zimenezo, ndinali ndisanamvetsetse zimenezo," Ndipo kenako anakamba zopukuta mmanja kupita kuchipinda, nagwada panso pafupi ndi kama wake, ndikumuuza Mulungu "Simdingachite ichi, "sindingakhale moyo uwu. Ndikugonjera kwa inu."

Ndipo email inapitilira, "Imeneyo inali miyezi inayi ndi theka yapitayo ndipo ndiloleni ndikuuzeni zimene Mulungu wandichitira mmoyo mwanga kuyambira pamenepo," **Mphamvu**.

Munayamba mwachitapo masewera owomberana ndi madzi kumpanda kwa nyumba ndipo wina nkuyamba kuombera ndi mfuti ya madzi. Mukakhala wa nzeru, mumachita chiyani? Mumatenga hosipaipi. Ndiye choncho ena atenga mfuti za madzi ndiye iweyo watenga hosipaipi. Komano, wanzeru akhoza kuchita chiyani, ngati iweyo watenga hosipaipi? Amathamangira kugwira hosipaipi ndi kuyipinda. Ndipo akayipinda, madzi amatuluka ochuluka bwanji? Palibe. Chimene ndikufuna kuti mumvetse ndi chakuti mukhoza kukhala Mkhristu wa mphamvu, wobadwanso mwatsopano ndi wokhulupirira mwa Yesu ndipo ngati hosipaipi yanu yapindidwa, ngati moyo wanu si ukugonjera, simumaona mphamvu Yake. Ndiye zonse zimakhala khalidwe ndipo kuyesera kukhala mmoyo womwe uli wasatheka ndithu.

Kukhala Mkhristu wa Aroma 12 kumayamba ndi ubale ndi Mulungu podzipereka kwa lye. Koma dziwani kuyambira ndime 2, ikuti, "Ndipo musafaniziridwe ndi makhalidwe a panso pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro." Pali lamulo labwino ndi lamulo loyipa, ndipo tikhazikika pa iyi ndi kukamba zokhudza ndimeyi.

Chofunikira ndithu, ndi chimene ikunena mokhudzana ndi mayendedwe a dziko lapansi, limakuuzani kuti ndalama ndi katundu ndi zogonana ndi mphamvu ndi ulemu zimabweretsa chitetezo ndi kufunikira ndi maubale otchuka. Akunena kuti, mukuyenera kutero mmalo mokhala moyo wodzipatula kuzinthu zaphindu za pa dziko lapansi. Koma

dziwani, sakunena kuti muyesetse kwambiri kukhala Mkhristu wabwino. Akunena kuti “mukhale osandulika.” Kenako mudzalawa ndi kumva zochitika. Kodi mukudziwa funso lalikulu mmoyo uno imene ndimeyi ikuyankha? **Kodi mmapeza bwanji chabwino kwambiri kuchokera kwa Mulungu?** Ndime 1 ikuyankha, “Kodi mungapereke bwanji chenicheni chimene Mulungu akufuna? Ndime 2 ikunena kuti, “Ngati Mulungu amandikondadi ndi kuti anandifera ine ndipo anauka kwa akufa, ali ndi dongosolo ndi moyo wanga.” Kodi mungagogode bwanji mmenemo? Tifotokoza kuchokera ku ndime imeneyi ndendende mmene imagwirira ntchito.

Ndipo chida chosowa ndimapeza mwa Akhristu ochuluka amene ndimayankhula nawo sikuperewera mphamvu kokha ayi chifukwa cha moyo wasadzipereka koma kusowa **mtendere**. Kuli Akhristu amene amaonera wayilesi ya kanema. Muyenera kupita kumene filiji ili. Mukalowa mugalimoto muyenera kutsegula wailesi ndi kuyika nyimbo chifukwa cha kufa, imfa nthawi zambiri imapangitsa kukhala osakhazikika.

Mudziko lonse lapansi, Pali malo ochepa amene ndi omvetsa chisoni kuposera Mkhristu wovomerezeka wotsatira Yesu wobadwanso mwatsopano amene Mzimu wa Mulungu amakhala mwa iye, amene amakhala moyo wakuti mwendo umodzi amayenda ndi Mulungu ndipo mwendo wina amayenda ndi dongosolo la dziko lapansi.

Ndine katswiri wa izi. Ndachita kafukufuku wozama. Ndikudziwa mmene zimakhallira kuti lachinayi usiku ndi kupezeka pa gulu losanthula Mawu ndipo lachisanu usiku kuyenda malo onse omwera mowa. Ndakhala zokhudza kudziletsa kuchita zachigololo ndipo nthawi yomwensho kumachita zadama ndikumuuza Mulungu kuti sindidzachitanso ichi, ichi ichi kapena ichonso.

Ndikuwuzani ine kuti ndinali Mkhristu womvetsa chisoni kwambiri mdziko lapansi kwa zaka zitatu zoyambirira nditakhala Mkhristu. Awa ndi malo amene okhulupirira ambiri amakhala. Timapinyulitsa mtendere wa Mulungu. Kudzimva kuperewera ndi manyazi okhala oyendayenda kudzimva kuperewera ndi manyazi pa zochita zadama/chiwerebere kudzimva kuperewera ndi manyazi pa mitundu yonse ya zinthu zosiyana zimene zimatinnyengerera pamene dziko lapansi limasanduliza maganizidwe anu kudongosolo losowa chuma limene limapereka.

Mulungu amatikonda ife kwambiri. Tiphunzira mmene tingadulire zimenezo; mmene Mzimu wa Mulungu ndi mphamvu za Mulungu zingatithandizireni kukhala moyo umene mumawulakalaka ndi umene iye amafuna kuchokera kwa inu. Ndipo tidzaphunzira kuti ndi mmene tingapezere zabwino kwambiri kuchokera kwa iye.

Kuyambira pa ndime 3 mpakana ndime 8, timaphunzira kuti muubale wathu ndi ife eni ake, Mulungu amakhumba kudziwunika modekha. Dziwani mawu akuti, “pakuti ndi chisomo cha Mulungu.”

Pomwe Paulo akuyika mulingo wa chiyezo ndi chilungamo ndi chimene zikutanthauza kukhala ndi uzimu weniweni chimene ndikufuna kuti mumve kuseri kwake ndi ichi chifundo cha mtima wachikondi. “Pakuti ndi chisomo chopatsidwa kwa ine, ndi uza munthu aliyense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyese, koma aganizire modziletsa yekha, monga Mulungu anagawira kwa munthu aliyense muyeso wachikhulupiriro.”

Akuyankhula za mmene mungapezere icho ndi mmene mulili gawo la thupi. Ndipo tidzazindikira kuti anasungitsa, mphatso ya mtengo wapatali mwa inu-ngati mungawone ndime 6 mpaka 8- tidutsamo kutsogoloko.

Koma Paulo akufuna inu ndi ubale wanu ndi inu eniake, kuyang’ana pa kalilole kuthupi wanu ndi kuyang’ana muuzimu ndi kuyang’ana pa ubale wa kalilole wa uzimu ndi kunena kuti. ”Ndikonda munthu uyu, Mulungu anawapanga iwo. Umunthu umenewo, mphatso zimenezo, msinkhu umenewo, maso amenewo, zolimbana nazo zimenezo ndi zokhudza mbiri ya banja lanu. Mu ulamuliro wa Mulungu, akufuna inu mukhale ndi maonekedwe enieni, odekha inu eniake.

Mu ndime imodzi imeneyo mawu akuti aganize modziletsa – akuwanena mnthawi zinayi zosiyana. Mulungu akufuna inu mudziwone eninokha mmene iye amakuonerani inu - wokodwedwa kwambiri, a mtengo wapatali ofunikira kwambiri, okhululukidwa. Kodi nanga mukudziwa funso lalikulu, limene likuyankhidwa? **Kodi mungathe kugwiritsitsa bwanji chenicheni chimene inu muli?**

Kodi mmazindikira kuti muli ndi nthawi ndi nyonga, ndi ndalama ndi kuziyimika ndi kukonza maonekedwe timachita monga munthu wina aliyense ngakhale ngati Akhristu, kuyesera kukhala ndi kudziyerekeza mwa anthu awa onse osiyanasiyana amene ndingati, “ndimakonda awa” ndi “ndimakonda awo” ndi “ndavala ngati awo” ndi “ndine wokongola ngati awo” ndi “ndikudziwa awa” ndi “kodi munadziwa kuti ndimawadziwa akuti ndi akuti” ndi “umu ndi mmene anthu ochuluka amanduzira zinthu” kapena “mwana wanga wachinya zigoli ziwiri mmasewera awo” ndi “ndikufuna kuti mudziwe kuti ndinaphunzira sukulu yapamwamba” ndi “chikwama ichi sichawamba, ndi chenicheni” ndi “wotchi iyi ndi yeniyeni siyokopera” ndi “ndakwezedwa pa ntchito...” Ndiye kenako mmaziika zonse muuzimu ndi kupita kosanthula baibulo ndi anzanu. “Chabwino malingana ndi ndemanga za mbukhu la wakutiwakuti pomwe ndimawerenga mawu a chigiriki pokonzekera nthawi ino yodzagawana mawu...” Hee! Timazichita timachita zonse, timachita, timachita. Gawo lino lidzaphunzitsa inu mmene mungazindikire kuti inu ndi ndani weniweni, ndiye kenako imapereka chida chosowa.

Ndime 1 ikupereka mphamvu pomwe mwaimvetsa. Ndime 2 ikupereka mtendere Ndipo ndime 3 ikukupatsani inu cholinga chifukwa Mulungu anapanga inuyo mwapadera. Ndinu ntchito ya manja Ake. Munalengedwa mwa Khristu Yesu mwa nthawi yake yabwino, asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi, lye anakudalitsani ndi mphatso ya inu yoti muchite china chake. Mu ulamuliro Wake Ali mu ubale umene wakhala ovuta mnjira zina ndi yopereka mphamvu mu njira zina.

Koma Mulungu ali ndi cholinga ndi moyo wanu. Pomwe nthawi zonse mukuyerekeza kukhala munthu wina kapena kuzifanizira inu eni ndi wina wake ndi kusavomereza kuti, ‘izi ndi zimene zili mphamvu zanga, izi ndi zimene zili zifooko zanga, izi ndi mphatso zanga, izi ndi zakumbuyo kwa moyo wanga, izi zimatulutsa zina zovuta ndi kudalira ena, izi zimatulutsa zinthu zina zazikulu koposa...’

Pokhapokha ngati mukhale ndikuyesa inu eni modekha, mudzakhala mukusewera masewero moyo wanu wonse. Mumayesera kukwaniritsa cholinga cha amayi anu, kapena cholinga cha abambo anu kapena cholinga cha miyambo yanu, kapena cholinga ya malo anu a ntchito kapena chimene anthu ena amaganiza. Kodi mumadziwa kuti ndi zomasula bwanji kumvetsa izi, “Ichi ndi chifukwa chake ndili pano. Cholinga changa ndi ichi. Ndipo ichi ndi chimene ndimachita bwino ndi ichi ndi chimene sindichita bwino. Apa ndi pamene ndikufunika thandizo ndipo apa ndipamene ndikufunika kutuluka ndi kumulola Mulungu andigwiritse ntchito.” Ndi zosithika ndi zosinthikandi ndithu.

Ndili ndi mnzanga wabwino ku Santa Cruz, California, ndipo anali wa zamalonda. lye amayanganira makampani akuluakulu kwambiri ndipo anawona kuti wayamba kukhala patali ndi akubanja ake ndiye choncho anaganiza kuti ayambe kupanga malonda a iye mwini wake. Anakonza masitolo pafupifupi 26 amene amagulitsa nsalu ndi zipangizo zosokera ndi katundu wam’nyumba, koma anawatchula dzina la mkazi wake chimene ndinaganiza kuti chinali chabwino kwambiri.

Ndipo anakhala munthu amene ndimaphunzira pansi pake. Ndinakhala naye nthawi yayitali ndipo amandithandiza. Ndinali wachisodzera muulendo wanga wokhala wodzifufuza ndekha modekha ndipo gawo limenelo lakumvetsa linali mphatso yanu yoyamba ya uzimu. Ndipo anali atadutsa kale muulendo umenewo.

Anthu ndi anthu. Ndipo mudziko lapansi lake anali munthu wamalonda wabwino. Anakhala munthu wopambana kwambiri. Pomwe mwapambana pa malonda mumapanga ndalama zambiri ndipo, anapanga ndalama zambiri. Anali mtsogoleri wabwino. Chifukwa cha ichi zaka zake zonse 25 za kukhala mu mpingo anatomikira mu mabungwe ambiri, misonkhano yambiri kumene aliyense amafuna kukamba za ndalama ndipo kenako kuwerengetsa ndalama pamapeto ake. Ndipo ngati makopedwe ofuna kupeza ndalama, kunali, “Dick, mupange ndinu.”

Ndipo anati, “ndinadana nazo zonse.” Ndipo tinayenda ulendo ndipo anazindikira mphatso zake za uzimu. Ndipo anazindikira chimene amakonda ndi kukhazikitsa zinthu, ndipo chimene amakonda kuchita ndi kuwapatsa anthu zida, ndipo chimene amakonda kuchita kubweretsa pamodzi malumikizandwe. Ndipo anati, “Kodi ukudziwa chiyani? Ndinangoganiza kuti ndisakhalenso mubungwe lililonse kapena gulu loyendetsa chinthu ichi chinali chiganizo cha uzimu.” Ananena, “Ichi ndi chimene ndichite.”

Ndipo moona mwake iye ndi amene anakhazikitsa utumiki wanga wa *Living on the Edge*. Anali maganizo ake Ndi munthu amene anayambitsa kuti uyende. Ndipo tsopano nditha kukuuzani mautumiki a mipingo isanu ndi itatu yosiyanasiana imene anakhazikitsa. Ndipo amangonena kuti kuli chimwemwe chachikulu mukadziwa mmene Mulungu anakupangirani ndi kukwaniritsa cholinga chanu.

Kodi mukudziwa chanu? Mwayamba kumva chimene ndikuyankhula ndi zosiyana kwambiri ndi “Chabwino, lero mmawa wa Lamulungu, ndi usiku wa loweruka kuyenera kupita ku tchalitchi. Eya, ichi ndi chabwino kwambiri, Eya, tikamva zimene tiyenera kuchita ndipo sindikuchita kwambiri. Ndipo ndiyesetsa kwambiri. Sizikuyenda bwino kwenikweni choncho ndiyenera kuonetsa ngati ndikuchita bwino kuposera mmene ndikuchitira pano. Ndine otsutsika ndithu. Eya, mnyamata, zambiri zochita, zambiri zochita.”

Kodi munazindikira moyo wachikhritsu wa anthu amene akugwira ntchito zina, ndipo kawirikawiri ntchito zimene sazikonda ndipo moonadi sakuchita bwino pa iyo? Ichi sichoona muuzimu. Uzimu weniweni ndi **waubale** ndi **wochitika** ndi **woyezeka**. Ndi anthu monga ife amene anapereka moyo wawo kwa Mulungu pa tsiku limene tinawoloka mzere umenewo, ndipo mokula timapatuka kuchoka pa zinthu zaphindu za dziko lapansi. Ndipo kenako timapanga kudzifufuza tokha modekha ndipo timazindikira cholinga chathu ndi chifukwa chiyani tili pano. Ndipo zimakhala zokondweretsa kuchokera pansi.

Chinthu chachinayi mukuona ndi chakuti ndi ubale ndi okhulupirira otumikira limodzi muchikondi. Kukhwima muuzimu kwenikweni ndi, “Chikondi chikhale chenicheni.” Mawuwa kwenikweni ndi “opanda kuvala chigoba kapena kunamizira.” “Dana nacho choipa; gwirizana naco chabwino. M’chikondano cha anzanu wina ndi mnzache mukondane.”

Kenako ndiye tipanga kabukhu konse, tidzamasula ndi kudzayankhula zokhudza kulemukezana wina ndi mnzake ndi kupatsana chikondi kwa wina ndi mnzake. Ndi chenicheni chokhudza anthu amene amadziwana kwenikweni ndi kukondana, ndikudzipereka kwa wina ndi mnzake ndi kupemphererana wina ndi mnzake ndi kuchita china chilichonse chothekera kuthandizana wina ndi mnzake. Ndikukhala ndi moyo wochita nawo zimenezo mmuphakati. Koma mmatumikira mwachikondi, ndipo ndi chikondi chenicheni. Simsonkhano umene ndimangopita. Ayi sichoncho. “chabwino, takwanitsa kusonkhana ku mapemphero a kutchalitchi katatu mwa kanayi pa mwezi uno. Ndikumva kukoma kuti ndachongetsa. Ndawerenga Baibulo kanayi musabata ino...”

Ndi zosiyana kwambiri zikafika pa ubale ndi Mulungu amene amakukondani inu kwambiri. Mumatsegula Mawu Ake ndi maganizo onthunthumira a chiyero, kuti Anakonda kwambiri ndi kuti amafuna kukuyankhula lero, ndi kuti amakonda kumva kuchokera kwa inu zimene zili mmaganizo anu ndi mumtima mwanu. Ndipo kwenikweni, Mzimu wake amakhala mwa anthu ena otchedwa Akhristu ena ndipo anayikiza mphatso mwa iwo, ndi kufuna kukukumbatirani kudzera mwa iwo ndi kufuna mukakhale oyankha mmalo mwawo kudzera mwa inu. Amafuna kukulimbikitsani kudzera mwa iwo. Kodi ndinu wokonzeka? Akufuna inu muchitenso choncho.

Ndipo pali chinthu ichi chodabwitsa mumpingo woyamba. Kumbukirani chimene Yesu ananena? “Lamulo latsopano ndikupatsani inu” - kwa ophunzira ake oyambirira, Yohane 13 – “kuti mukondane wina ndi mnzake” - bwanji --- “monga ine ndakondera inu. Pa ichi” - osati pomanga nyumba osati pa chikhaliidwe chowirikiza - “pa ichi dziko lidzadziwa kuti Atate anandituma ine, pa mmene mungakonderane wina ndi mnzake.”

Ndipo gawo ili la uzimu weniweni kuchokera pa Aroma 12 likuyankha funso limene tonse timalimbana nalo - **Kodi ndikumane nalo bwanji gulu laphakati leneleni?** Pali anthu ambiri amene ali wokha sindikutanthauza kungokhala mugulu sindikutanthauza kungokhala membala wa chinachake. Ndikutathauza kuti ndi pati pamene ndingakhale ndikumva kuti wina wake kapena awiri kapena atatu mmoyo wanga ndingathe kumasula za mtima wanga ndi kudziyika pachiwopsezo ndi kuwauza iwo zinthu ndipo sindingaweruzidwe ndipo adzatithandiza ndi kundikonda. Ndipo ngati ndikudutsa mnyengo zowawitsa, adzakhala nane ndipo akudziwa kuti nanenso ndidzakhala nawo.

Kukhala ndi abwenzi enieni - osati ongoyerekeza chabe - osati ongophiphiritsa - abwenzi amene angafe mmalo mwanu. Uwo ndiye mphakati weniweni. Ndipo ndikuuzani chiyani. Pamene mwazungulidwa ndi anthu amene amakondana motero, ndi za mphamvu.

Kodi mukudziwa chimene chikusowa mmoyo mwa Akhristu ambiri? Simphamvu zokha, sicholinga chokha. Kodi mukudziwa chimene chikusowa mwa Akhristu ambiri? Kukumana ndi **kupezeka kwa Mulungu**. Timachita zinthu ndi kuyembekezera Mulungu achita ichi kapena icho ndi kuganiza kuti ali apo, pena pake, mwina mwake, njira ina yake. Kodi mumadziwa dongosolo loyambirira la Mulungu kupatula pomwe mwawerenga Mawu Ake kapena pamene mukuyankhula naye kapena kulingalira? Kodi mukudziwa njira yake yoyambirira yodziwonetsera kupezeka kwake? Ndi kudzera mwa Akhristu ena.

Ngati mngelo wa Mulungu angabwere mkati mwa usiku kumiyendo ya kama wanu lero usiku, chonde ndiwuzeni zokhudza icho. Ndipo ngati mngelo wa Mulungu akukumbatirani inu ndi kukukonzerani inu chakudya ndi kunena, “Tandiuzeni chenicheni chimene chikudutsa mkati mwanu chifukwa ndikufunitsitsa kuti ndimve chifukwa ndimasamala za inu.” Mulungu akudalitseni.

Koma 99.9% ya ife tonse, mmadziwa mmene Yesu amaonetsera mmoyo mwanu? Adzadzionetsera muthupi la munthu wina. Mwamuna kapena mkazi kapena wophunzira naye mnzathu pamene pali mankhwala awa, ndipo ndi chitetezo, ndipo ichi ndi chikondi, ndipo mwadzikhuthula kwa wina ndi mnzake muchikondi cha paubale, ndipo mumapatsana chikondi chopambana mwa ulemu ndipo mmakhala moyo limodzi.

Gawo lomaliza lokhala Mkhristu wa Aroma 12 siubale okha ndi Mulungu, kapena ubale wanu ndi dziko lapansi kapena ndi inu eni nokha, Kapena okhulupirira, koma ndi zoipa za mdziko - maubale ndi osakhulupirira amene amakhala a ukali ndi Uthenga Wabwino. Ndipo mwatsoka, nthawi zina ndi woipa ndi owopsa kwa inu. Koma ndi kuchita mopitilira nzeru za munthu pothana choipa ndi chabwino.

Imvani mtumwi Paulo. Mungathe kumumva iye akulalikira Uthenga wa pa Phiri ndi Mzimu wa Mulungu. “Dalitsani iwo akukunzuzani inu. Dalitsani osatemberera. Musabwezere, okondedwa, koma siyirani mkwiyo wa Mulungu. Kubwezera ndi kwanga, Ndidzabwezera.” Ngati mdani wanu ali ndi njala Kodi mumachita chiyani? Mudyetseni. Ngati m’dani wanu ali ndi ludzu, Kodi mumachita chiyani? Mpatсени chakumwa. “Musagonjetse ndi choipa.”

Tonse ndife anthu choipa chidzabwera mmiyoyo yathu muulendo wathu wapadziko lapansi. Enanu mwakhala nacho kuposera ena, mudzang’ambidwa, mudzakhomereredwa, mudzakhala ndi anansi amene adzakuthaweni, mudzakhala ndi ana amene adzayankhula zoipa kwa inu. Anthu amene anabwereka ndalama kwa inu ndi kulonjeza kuti adzakubwezerani ndipo taonani - sadzakupatsani.

Pali choipa chimene ndi chadongosolo. Mungathe kukonda Mulungu ndi mtima wanu wonse komabe Akhristu okonda Mulungu ndi mtima wawo onse amadwala matenda a khansa. Amawombedwa ndi oyendetsa galimoto oledzera. Amaluza nyumba zawo chifukwa chakuwonongeka kwa zachuma. Ndipo akhala okhulupirika ndi ndalama zawo choipa chikubwera mnjira yanu.

Choncho kodi uzimu weniweni ndi chiyani? Ndimakonda chimene Mulungu amanena - uzimu weniweni ndi mmene Mzimu wa Mulungu amakhalira moyo wa Khristu mu ubale ndi Atate wanga Wakumwamba, ndi dziko lapansi, ndi ine mwini wake, ndi okhulupirira, ndiye kenako ndi wosakhulupirira pomwe zinthu zopanda chilungamo zifika pa njira yanga.

Funso limene likuyankha ndi, “**Kodi mmagonjetsa bwanji choipa chimene chalunjika kwa inu?**” Chinthu chimene Akhristu ambiri asowa mmoyoyo yawo ndi **kaonedwe**.

Tikhoza kutenga khadi ya 3 x 5 kapena kutenga lamya yanu ya mmanja, ndi kudina pa malo pamene panena kuti notsi ndipo tikhoza kulemba ndandanda wa anthu anayi kapena asanu amene ankayenda ndi Mulungu amene sakuyendano ndi Mulungu tsopano - oyenda naye atawasiya iwo, galimoto itawonongeka, atachotsedwa ku ntchito. Zoona?

Onani pali chifukwa chimene 25% la bukhu la Genesis linakhuthuridwa ku moyo wa Yosefe, chifukwa chakuti Yosefe ndi chithunzi cha uzimu weniweni, cha mmene mungachitire ndi choipa cholunjika kwa inu. Ndipo sizinali zophweka - anaperekedwa, ananamiziridwa, anayiwaliidwa, anagulisidwa. Koma awo ndi mawu ochepa - “Ambuye anali ndi Yosefe.” Kodi mukudziwa chimene Yosefe anali nacho? Kaonedwe.

Yosefa anatenga - ngakhale analibe zimenezi mmasiku amenewo - ndege ya kaonedwe ka uzimu pomwe iye anali mundende kapena kunamiziridwa anapitiliza kuyitenga ndege imeneyo mmwamba mwenimweni ndi kuyang'anira panso zonse ndi kunena. “Kodi mukudziwa china chake? Kuli Mulungu wolamulira amene analamula kapena kulola ichi, ndipo amandikonda, ndipo sindikudziwa kuti zidzayenda bwanji koma ngati sindingamasulidwe koma mmalo mwake ndikukhulupirira iye. Adzachichitira ku ubwino wanga ndipo adzachita mwa ine ndi kudzera mwa ine chimene sichikadachitika. Ndikukana kukhala owawidwa mtima, ndikukana kusakhululukana, ndikukana kukhala wozunzidwa, ndikukana dziko lapansi kundiwumba ine. Ndidzakhulupirira Mulungu wanga chifukwa ndili ndi kaonedwe.

Ndipo Yosefe ananena kwa achimwene ake, kumapeto kwa bukhu,” munandipangira ine choipa koma Mulungu anachipangira chabwino.” Ngati zinthu izi zonse zovuta sizidakachitika, sakadakhala munthu wachiwiri wamphamvu zambiri mudziko lapansi ndipo sakadapulumutsa mtundu wa Ayuda.

Ndipo Mulungu ali ndi dongosolo lanu ndipo muli ndi nkhani ya Yosefe kuti mukhale.

Kodi mwayamba kumva kuti uzimu weniweni ndi ukukhudza chiyani? Ndi okhudza ubale. Ndi choyezeka. Mungathe kuyeza “Kodi ndinadzipereka? Kodi ndine olekanitsidwa kuzaphindu za dziko lapansi? Kodi ndili ndikudzifufuza modekha? Kodi ndikutumikira mwachikondi? Kodi mwauzimu ndikuthana ndi choipa ndi chabwino? Ukuthandizeni kufunsa ndi kuyankha mafunso amenewo.

Pang'ono ndi pang'ono, pomwe tikuyenda pamodzi kudutsa umu - ndipo pomwe mukukhulupirira ndi kumvera mwachikhulupiriro - mudzayamba kumva **mphamvu** ya Mulungu, **mtendere** wa Mulungu, **cholinga** cha Mulungu, **kupezeka** kwa Mulungu, ndi **kaonedwe** ka Mulungu. Yesu akunena kwa ife, “Ngati mukhala mwa ine ndi mau anga akhala mwa inu,” ndipo Mawu amenewo akungotanthauza kuti ngati mukuwatenga ndi cholinga mochigwiritsa icho mwachikhulupiriro mudzadziwa choonadi - “Ndipo mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakumasulani.”

Ndikufuna kutseka gawo ili ndi kaonedwe kofunikira kwambiri. Pali chowopsa mu ulendo wathu. Monga ndi ulendo uliwonse pali zowopsa. Koma pali pa ulendo wathu kuti mochenjera kuyamba kuganiza mwa ulendo wa Aroma 12 monga kachitidwe ka makhalidwe abwino ndi kuyika zotchinga zokhalira moyo.

“Chabwino, ndidzaperekedwa ndidzakhala olekana, wodzifufuza modekha. Ndikuganiza kuti ndinazimvetsa. Ndidzatumikira mwa chikondi ndi ...sindingathe kukumbukira chomaliza..... mwauzimu kuchita ku chinthu china ndi chinthu china.” Ndi kuchitembenuza icho mu chinthu chimene mukuyesetsa kuchipewa.

Ndikufuna kukukumbutsani kuti uzimu weniweni sukugwirizana ndi kukhala moyo wabwino koteru kuti Mulungu adzakukondani inu. Uzimu weniweni uli ndi chilichonse chofunikira kuyamba kumvetsa kutalika ndi kuzama ndi muutali ndi muufupi wa mmene Mulungu anakukondani inu kale anasonyeza chikondi chimenecho ndipo inu mukukhala moyo womasuka wa chikondi chimenecho.

Mumanotsi ndinalemba chitchati chabukhu lonse la Aroma. Mitu 1 mpaka 3 amatiuza kuti tonse tinaperewera pa ulemerero wa Mulungu. Timazikometsa izi. Ichi sichongokhala kuti, “Si iwe munthu wabwino.” Tachimwa Tamupereka Mulungu. Ndife anthu amene tinamuukira Mulungu. Ndife anthu amene tinamuukira Mulungu ndi iye ndi oyera ndi mkwiyo wa chilungamo chake uli pamphumi pathu pachifukwa cha chimene tachita. **Tchimo.** Ili ndilo vuto lathu limene limatisiyanitsa ife kuchoka kwa Mulungu.

Mmitu 4 ndi 5 muli yankho. Yankho la tchimo ndi **chipulumutso.** Yesu munthu wathunthu, Mulungu wathunthu anakhala moyo wangwiro, anafa pamtanda kulipira machimo anu ndi kuuka kwa akufa ndi kupereka mphatso yaulere kwa aliyense amene angakhulupirire ndi kuchilandira.

Mitu 6 mpaka 8 akupitiriza kulakhula zokhudza mmene moyo uwu watsopano umakhalira. Sikachitidwe kamakhalidwe abwino. “Yesetsani.” Mmalu mwake Paulo anati “Mzimu wa Mulungu wa Moyo mupangano latsopano adzatenga malo mkati mwa thupi lanu la umunthu.” Atatha kukuchotsani inu ku ufumu wa ku midima. Anakuyikani mmalo mwake ku ufumu wakuwala. Mzimu wake umatenga malo, ndi kupezeka kwa moyo wa Khristu ndi mphamvu ya Khristu kudzera mmawu a Mulungu ndi la anthu a Mulungu amene anabereka.

Momveka bwino, Paulo akukamba za “mpakana Khristu apangidwe mwa inu.” ndipo ichi chimatchedwa **kuyeretseka.** Ndipo ndi ulendo, woti munayenda mopita kutsogolo sitepe imodzi ndi kubwerera mmbuyo masitepe atatu, ndiye kenako ndikupita patsogolo ndi kubwerera ndiye kenako ndikupita patsogolo. Koma mumakula.

Ndipo kenako pamapeto, Paulo anawakumbutsa Mulungu nthawi zonse amasunga malonjeza Ake. **Kudzipereka.** Timakhala molimba mtima chifukwa Mulungu amawongolera ndi kusunga malonjezo Ake. Paulo akuchinena mu Aroma 9 mpakana 11 kuti malonjezo a Mulungu kwa Ayuda adzakwaniritsidwa ndi kuti iwo anafwambula mpira munjira yosamala udindo wawo kwa Mulungu. Choncho iye akuti “Ndidzawatulutsa iwo mmasewero ndi kukwaniritsa chili chonse chimene ndinalonjeza kwa Abraham ndi kwa Davide, koma mpingo udzakhala chotengera madalitso Anga mpaka ndidzanene kuti nthawi yatha ndi kubweretsa kutseka kwa mbiri ya masiku otsiriza.”

Ndipo atatha mutu 11 cha kusatengera kumene mumakhala, Mulungu amakukondani, anakuferani inu, anayika Mzimu wake mkati mwanu ndipo adzasunga lonjezo lililonse tikufika pa Aroma 12 - “Chifukwa chake ndikupemphani abale “ Chiyani? “Mupereke matupi msembe yamoyo.”

Ndikufuna ndikufunsi inu, Kodi munayamba mwasiya chikhulupiriro chanu mwa Khristu inu ngati munthu panokha kuti akukhululukireni machimo anu? Chifukwa chimene ndaona nthawi ndi nthawi ndi chakuti anthu moona mtima kawirikawiri amayamba kubwera ku mpingo ndipo mopanda chikumbu mtima amaganiza kuti “Ndikuyesetsa kukhala munthu wabwino” ndipo amayamba kuwona kusintha. Koma chimene nthawi zina sazindikira ndi chakuti mmasowa, pa tsiku lina, pa nthawi ina, kubadwanso kwatsopano. Ndipo izi ndi zakumbuyo ku Mutu 3 wa Aroma ndi koyambirira kwa Mutu 4 kumene mmabwera kwa Mulungu pa tsiku longa la lero ndi kuvomereza moona mtima kuti, “Mulungu ndikufuna thandizo lanu, ndachimwira Mulungu oyera. Lero, ndakhulupirira kuti mwazi wanu unalipirira machimo anga ndi kuukanso kwanu kunatsimikiza kuti ndi zoona ndipo pa tsiku ili, ndikufuna kukupephani kuti mubwere mkati mwa moyo wanga mpaka muyaya, kundikhululukira ine ndi kukhala Atate wanga.”

